

MWA CHIKHULUPIRIRO, MOSE



Zikomo inu, M'bale Neville. M'mawa wabwino, abale. Ndi chabwino kukhala tiri pano lero pa kachisi. Ndipo ine ndimaganza kuti mwina ine ndikanamutenga M'bale Neville kuti alankhule mmawa uno, ine ndiyesere usikuuno. Ndiyeno ine ndimayang'ana ndiye ku phunziro la Sande sukulu la m'mawa uno. Ndipo chiani... Ambuye akalola, ife tiyesera ku—kuti tikhale ndi phunziro la Sande sukulu ili.

² Tsopano, akhala ali masabata awiri tsopano, pafupifupi, chibwererani kuno. Ndipo ine ndakhala ndiri wamanjenje kwambiri monga inu munamvera, kuti, kolalikirira uko, ine ndinatopa kwenikweni, kwenikweni ndipo sindinathe kuti ndizipitirira mulimonse. Ndiyeno ine ndimayenera kuti ndingobwera kudzapuma pang'ono. Ndipo ine ndinatenga pafupifupi masiku atatu kuti ndikafike ku Wolf Creek Dam, uko mu Kentucky, kumene ine ndinabadwirako. Ine ndinaganiza, "O, ine ndikumverera bwino basi tsopano. Ine ndiri bwino.

³ Ndipo ine nditabwerera kunyumba, ndipo chinthu choyamba chaching'ono chimene ndinakumana nacho pamaso chinali chokhala ngati nkhani ya boma ya msonkho. Ine ndinapita njira yonse mmusi kachiwiri. Chotero ine ndinazindikira kuti zinditengera kuposa sabata imodzi kapena awiri kuti ndithe kupuma.

⁴ Ndipo utumiki wanga ukukonzekera kuti usinthe tsopano. Ndipo ine ndiribe misonkhano imene yakonzedwa. Ndipo ndicho chifukwa chake ine ndinakhala ngati ndangopatukapo, ndi kuganiza, ndipo tsopano kwa masabata angapo otsatirawa, ine ndingopuma, kupuma kwathunthu, ndi kumayembekezera pa Ambuye.

⁵ Ndipo ambiri a anthu inu pano, amene muli apakale, amene mwakhala muli ndi ife motalika kwambiri, mukukumbukira zomwe Ambuye ananena kwa ife. Iye nthawizonse wakhala akuchita zomwe Iye ananena kuti Iye akanadzazichita.

⁶ Ndikukumbukira, pamene pachiyambi pomwe, mu tchalitchi pano, m'mawa umene ife tinkaike mwala wa pa kachisi, momwe kuti Iye... Izo zinalembedwa, ndipo ziri mkati mwa mwalawo, pa tsamba la Baibulo langa. Mmawa uja, masomphenya aakulu aja, anati, "Uyu si kachisi wako."

⁷ Ine ndinati, "Ali kuti iye, Ambuye?" Ndipo Iye anakandikhazika ine uko pansu pa mlengalenga. Ndipo Liwu linadza. Ndipo ine ndinayang'ana ndipo ndinaiwona mitanda itatu iyo, yonga, mitengo ndi chipatso cha iyo, zina zotero. Inu mukudziwa chimene masomphenyawo ali. Izo zakhala zitalembedwa, kwa zaka.

⁸ Ndikutenga, tsiku lina, bukhu lakale pamwamba apo, ndikuwerenga zina za zinthu zomwe Ambuye anali atanena, anazineneratu; zinakwaniritsidwa kale. Zokhudza nkhani ya ana iyi, ndi momwe nkondo iti idzabwerere, ndipo zinthu zonse izo zachitika.

⁹ Zinthu ziwiri zokha zatsalira, mwa amodzi a maulosi aakulu amenewo. Zimenezo ndi zakuti, magalimoto odziyendetsa okha adzakhala ali pa msewu, owoneka ngati dzira, kokha kuti iwe sungaiyendetse iyo. Iyo ndi yomadzilamulira yokha. Ndipo kenako padzakhala mkazi wamphamvu ati adzauke, chifukwa Amereka ndi fuko la mkazi. Ndipo lidza . . . Mkazi wamphamvu adzauka, ndipo adzakhala Puzidenti kapena chinachake chonga momwemo, mu fuko. Ndipo zikadzatero padzabwera kuthetsedwa kwathunthu. Fuko lonselo lidzasesedwapo.

¹⁰ Ndipo, izo, ine ndikuneneratu . . . Tsopano izi si Ambuye akunena izi. (Zina zija, za mkazi, izo zinali, zinali Ambuye.) Koma ine ndinaneneratu, mu 1933, kuti dziko likanadzakumana ndi kuthetsedwa kwathunthu isanafike '77.

¹¹ Kotero, ine sindimadziwa pa nthawi imeneyo kuti anali nacho chinachake chimene chikhoza kulithetseratu ilo monga ali nacho tsopano, koma ine ndinaliwona fuko mu kuthetsedwa kwathunthu, linangotsala zitsa za mitengo ndi zinthu monga choncho, zitatsalirapo.

¹² Kotero, izo ziri panjira yake. Ndipo ngati zinthu zina zonse izi zafika pochitika monga Iye ananenera, nazonso zichitika; ndipo basi monga Iye ananenera mu Lemba apa, zimene Iye akunena. Ngati Khristu anabwera nthawi yoyamba, Iye adzabweranso nthawi yachiwiri. Ndi zinthu zonse zomwe Iye ananena kuti zidzachitika. Ndipo mchiyembekezo tikuziwona izo, ndipo tikudziwa kuti tiri . . . nambala yathu yatsala pang'ono kuti itchulidwe, ngati fuko, tikudziwa kuti Mpingo watsala pang'ono kuti utenge Mkwatulo Wake. Izo zimasuntha mtima wa mtumiki, kapena aliyense wa mamembala, kudziwa kuti ife tiri mu tsiku lino ndi nthawi yomwe ife tiri kukhalamo. Ndi nthawi yopambana imene munthu aliyense anayamba wakhalapo pa dziko lapansi, ndi pakali pano; imeneyo ndi, kwa Mpingo. Kotero, ine ndithudi ndikusowa mapemphero anu.

¹³ Ndiyeno ine ndawona mu kachisi, ndipo ine ndawona kuti iwo anali . . . akhala ndi kusankhidwanso kwina ndi chirichonse, mu mpingo, kwa mabodi ena ndi zina zotero.

¹⁴ Ndipo—ndipo mpingo umafunika kuti ukhale ndi msonkhano waung'ono, kukondoweza pang'ono. Ndipo inu nthawizonse mwakhala muli abwino kwa ine, ndipo mwandidalitsa ine. Ndipo ine kukhala pano, zikuwoneka kuti ndi mdalitso kwa inu. Ndipo ine ndikutsimikiza, kuti kukhala ndi inu, kwakhala mdalitso kwa ine. Ndipo inu nthawizonse mwakhala mukuvomereza zomwe ine ndimanena kukhala

Choonadi, monga ine ndikuziwonera izo kudzera mwa Mulungu. Ndipo i—ine ndikuyamikira zimenezo.

¹⁵ Kotero ndiye, ine ndinayambapo, ndiyeno ndinali woti ndifufuze, ndi kuwuwongola mpingo wathu, mu mabodi ake, ndipo kenako zisankho ndi zina zotero. Ndiyeno—ndiye, ine ndimaganza, zikatha zimenezo, ine ndipita uko ndi kukapuma pang'ono ndisanabwererense ku malo a ntchito kachiwiri.

¹⁶ Muzisunge izo mwanokha. Tsopano, izi si za akunja. Ndi za kachisi uyu. Ife tikufuna kukhala ndi msonkhano ndi kachisi uyu, kotero kuti chirichonse, ndi cholakwika chirichonse, zinthu zonse zomwe zakhala zikumapitirira, ndipo mwinamwake zoganizirana pang'ono kwa wina ndi mzake; zimenezo, ine ndimutenga wina aliyense wa iwo ndi kuwabweretsa iwo pamaso ndi pamaso. Kotero ngati inu simukufuna kuti mukomane nazo izo, inu kuli bwino muchokeko kuno; chifukwa inu mukomana nazo maso ndi maso ndi chirichonse cha izo, monga mmene ife tinkachitira kuno ku kachisi. Ndipo zonsezo zisalazidwa, chifukwa ndife abale ndi alongo amene timanyema mgonero, Thupi la Khristu, pa gome la madalitso. Ndipo si china koma Mdierekezi yemwe angapange china chirichonse chomwe chingakhale cholakwika, ndipo yemwe angapangitse zoganizirana, kapena kukhadzulana, kapena chirichonse chonga zimenezo. Ndipo ine ndimutenga M'bale wathu Neville, ndipo ife tizipita malo ndi malo, ndi kuwabweretsa anthu kwa anthu, limodzi, kufikira kachisi wakale atabwerera, atakhazikitsidwanso kachiwiri, atakhala pa mapazi ake, kuti azipitirira mtsogolo kwa Ufumu wa Mulungu. Tsopano, ichi ndi, chifukwa chimene ine ndanenela izi, ndi chifukwa chakuti izi zikuchitika ndi kagulu kathu kakang'ono kuno m'mawa uno.

¹⁷ Ndipo tsopano ine ndipita ndikapume, ndipo ndidzabwereranso mwamsanga mmene ine ndingathere. Ndiye ine ndikuyembekeza kuti ndichoka kupita ku malo antchito kawirinsu. Ndipo nthawi ino, Ambuye akalola, ine ndikufuna kuti ndidzatenge zapang'ono zomwe ife tazonkhanitsa mu ndalama, ndi zina zotero, za inemwini, uko mu...dongosolo la mishonare yakunja iyi. Ndi kukagula tenti yatsopano, ndi zida zina zatsopano, ndi kuuyambapo waku malo antchito. Osati kumapita tchalitchi ndi tchalitchi, koma tikupita ku misonkhano yathu yathu.

¹⁸ Tsopano, sikuti ndikunyozeza abale amene andiitana ine, zomwe zili zopambana. Koma zambiri za izo, inu mumapeza kuti misonkhano imeneyi, iwo amati inu mukakhala uko, ndiyeno amzako onse amabwerako, ndiyeno pamakhala kumemeza kwakukulu kofuna ndalama. Zimangowakolola anthu amenewo. Ine ndangoyamba kuzindikira zimenezo, inu mukuona. Kotero izi—izi si zabwino. Ife tikufuna kuti tikhale ndi malo omwe tingawabweretse iwo. Inu simukusowa kumadzabweretsa

ndalama zanu. Mudzangobwera chomwecho, inueni, ndi—ndi kudzawatumikira Ambuye. Mwawona? Ndi kotero tsopano . . .

¹⁹ Ndipo utumiki wanga wasintha pakali pano. Inu mukukumbukira pamene ine ndinkachita kugwira dzanja la munthu, ndi kungoyima pamenepo, ndipo Ambuye amandiuza ine chomwe chinali vuto lawo. Anati, “Ndiyeno zidzafika pochitika, kuti iwe uzidzadziwa chinsinsi cha mtima wa anthu.” Wina aliyense wa inu akudziwa kuti zimenezo zimachitika mwangwiro basi momwe Iwo ananenela. Tsopano iyi ndi sitepe yotsatira, yomwe yaneneredwa ndi kuloseredwa, yomwe iti ikhale kutali kwambiri kuposa ina iliyonse ya Iyo, inu mukuona. Ndipo izo zikusinthika pakali pano.

²⁰ Ndipo ndicho chifukwa chake Satana akundimanya ine ndi za msonkho, akuyesera kuti azindiuza ine, boma, kuti ine ndiri ndi ngongole ya msonkho pa ndalama iliyonse yomwe ine ndatengapo, ngati mtumiki, kuchokera mu zaka twente-seveni zapitazo, ndinalowa mu utumiki. Sizili chomwecho, chifukwa izo zimadutsa pa mpingo pano.

²¹ Ine ndine trasti wa mpingo uno. Izo ndi zoona kwenikweni. Izo zinalembedwa apa. Kotero, ndiye, ngati ine ndili trastimsungichuma wa mpingo uno, ndiye palibepo kalikonse mu dziko . . . Boma liribe chochita ndi zimenezo. Iwo sakufunsa mpingo. Iwo akundifunsa ine pokhala msungichuma wa mpingo. Ndipo matrasti asayina pepala limene liri kuma banki uko, kuti ndalama zanga zonse . . . Mmaloko mokhala ndi bungwe loyendetsa ndalama ine ndimazidutsitsa izo mu mpingo wanga kuno, chifukwa iwo ndi wokhazikika kale ndi kale, mulimonse.

²² Ndipo kuti ndichite zimenezo, zimandithandizira ine kuti ndisamachithawe tchalitchi ndi kuchisiya icho, ndi kumapita kunja ndipo osakhala kanthu kuno. Ine nditatha kuwalonjeza anthu kuti ine ndizibwerera ku tchalitchi, nthawi ndi nthawi, ndi kudzawathandiza iwo. Ndi chifukwa chake ndinazisiya izo monga choncho, chifukwa ine ndinapanga lonjezo kwa anthu inu. Ndi chifukwa chake ine ndimakhala nacho icho mwanjira imeneyo, mmaloko mokhala ndi munthu payekha. Ndiye, ngati iwe uchita zimenezo, izo zimaponyera izo ku bungwe. Ndipo ine molimba ndimatsutsana ndi bungwe. Kotero i—ine ndizisunga izo momwe izo ziliri, mmanja a Mulungu, kuti tikathe kuyendabe chitso golo kwa Ufumu wa Mulungu.

²³ Tsopano, mmawa uno, ife tikufuna kuti tiwerenge Mawu odala akale awa, ndi kuwakhulupirira.

²⁴ Tsopano, ine ndikufuna kuti ndinene, apanso, ine ndikumuwona M'bale Egan ndi ambiri, ena a matrastii akhala pano. Ife titatha kukhala ndi msonkhano wathu wa matrasti, usiku wina; izo ndi zoona, ine mosabisa pamaso pa mpingo, kuti wina aliyense wa inu simuli ma—matrastii ochita kuikidwapo.

Inu ndi matrastii ochita kusankhidwa, ndipo dzina lanu liri pa mabuku. Chabwino.

²⁵ Ndipo tsopano akhala ndi zisankho zinsano za—za madikoni, ndi ena otero. Ndipo M'bale Neville ali, akhala akuwaitana iwo ukangotha msonkhano uno, chabwino, ndi msungichuma ndi ena otero, pamene ife tikuwukhazikitsa mpingowu. Kuwuyikira, maziko onse, kukonzekera, tikatero tikhoza kukhala ndi chitsitsimutso pamene chikubwera.

²⁶ Tsopano, tisanatembenekire ku masamba apa, ku phunziro lathu la Sande sukulu, kwa Mawu opambana awa a Mulungu wa moyo; tiyeni ife tingoweramitsa mitu yathu, mphindi pang'ono, pamene ife tikulankhula ndi Mlembi wa Bukhu ili. Ndipo tsopano muike kumbali ganizo lirilonse, chirichonse chomwe chiri chosiyana, chokulepheretsani inu kuti mukhale ndi m'dalitsa.

Tiyeni tipemphere.

²⁷ Mulungu woyera kwambiri ndi wolungama, mu Kukhalapo kwanu kodala ndi kwaulemu ife tikubwera tsopano, tikupereka kwa Inu miyoyo yathu, ndi—ndi miyoyo yathu, ndi matupi athu, ndi zintchito zathu, ndi luso lathu. Ndi zonse zomwe ife tiri nazo, ife tikuzipereka izo kwa Inu. Ndipo pamene Inu mukuyang'ana pa ife, Ambuye, ngati liripo tchimo lirilonse losaphimbidwa ndiponso losalapidwa, ife tikukupemphani Inu, O Ambuye Mulungu, kuti Inu mukayikepo Magazi a Mwana Wanu, Yesu, pa malo amenewo. Pakuti, tikuzindikira kuti ife mwa tokha tiri osakwanira, ndipo pamenepo ndi zosatheka kuti ife tingakhale odzidalira tokha. Koma ife tikudalira kwathunthu pa Magazi Ake ofunika, ndi chisomo Chake kuti akayike pa chiwerengero chathu, kuti ife ochimwa osayenera tikakhoze kubwera molimba mtima tsiku lina kudzafika mu Kukhalapo Kwanu, kubweretsa pamaso pathu Magazi awa a Ambuye Yesu. Amene, Inu, mu nthawi za mmbuyomu, munawazindikirapo iwo kukhala Magazi a Mwana Wanu wobalidwa yekhayo, ndipo munapanga lonjezo, lakuti, “Kudzera mwa Iye, ngati ife tilapa machimo athu, ife tidzalungamitsidwa mwa chisomo Chake.”

²⁸ Ndipo tsopano ife tikupempha, Ambuye, kuti Inu mutikhululukire ife cholakwitsa chirichonse, tchimo lirilonse la kulakwitsa kapena kuchotserapo, mphulupulu, kuti ngati lingaliro lirilonse loyipa lapyoza moyo wathu, ndi mivi yowopsya ya mdierekezi, kuti Inu mumuthamangitsire kutali mdani Wanu woyipa yu, ndi wa anthu Anu.

²⁹ Ndipo ife tikupempha kuti Inu mutumize Mzimu Woyera kuti udzawagwire Mawu pa nthawi ino, pamene ife tikudzipereka tokha ngati zida, kuti Inu mulankhulire kudzera mwa ife, ndi kumva kudzera mwa ife, Mawu Anu. Ndipo mulole kuti ife pobwezera tidzawalandire Iwo kuti akuchokera kwa Inu, ndipo tichoke pamalo pano, lero, tikumverera kuti

takonzedweranso ku ntchito ya Khristu; kuti tikakhoze kukhala okonzekera utumiki wa usiku uno ndi mawa, chifukwa cha kuchezeredwa ndi Mzimu Woyera.

³⁰ Muwadalitse abale athu konsekonse, matchalitchi pa dziko lonse, amene akugwiritsitsa Mawu a Moyo mu tsiku loipa lino. Ife tikumverera kuti palibe nthawi yambiri imene yatsalira kuti tigwire ntchito, pakuti usiku ukubwera mwaliwiro. Mitambo ya nkhondo ikuyandama kachiwiri. Choipa chiri pafupi, ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutilore ife tigwire ntchito ngati kuti sitinayambe taigwirapo. Mupumitse matupi athu otopa, Ambuye, ndipo mutibwezeretsenso ife waku nkhondo. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Ambuye Yesu, ndipo chifukwa cha Iye ife tikupemphera. Amenii.

³¹ Pamene ife tikutsegula, mmawa uno, Baibulo, ku—ku mutu wa 11 wa Bukhu la Ahebri.

³² Lachitatu usiku ife tinali kulankhula pa mutu wa 7 wa Bukhu la Ahebri, za “Melkizedeki, kukhala wopanda bambo, ndi wopanda amayi, wopanda chiyambi cha masiku, kapena mathero a moyo.”

³³ Ndipo ine ndinaganiza, mwinamwake, mmawa uno, zikhoza kukhala zoyenera kuti nditsegulenso Bukhu lodabwitsa ili, pokhala kuti ife tiri nawo maziko a zimene ife tikufuna kuti tinene, mu zomwe timawerenga mmbuyomu. Ndipo polumpha mutu wa 10, ndi mutu wa 9, umene uli malamulo a kupereka nsembe, ife tifika pamalo a “chikhulupiro.” Ndipo apa mu Bukhu la Ahebri, mutu wa 11, ndipo kuyambira ndime ya 23, ife tikuwerenga Iwo monga chonchi.

Mwa chikhulupiro Mose, pamene iye anabadwa, anabisidwa miyezi itatu ndi makolo ake, chifukwa iwo anawona kuti anali mwana woyenera; ndipo iwo sanawope chilamulo cha mfumu.

Mwa chikhulupiro Mose, pamene iye anafika kukhala wausinkhu, anakana kuti adzitchedwa mwana wa mwana wamkazi wa Farao;

Anasankha mmalo mwake kuti amve kuwawa mazunzo limodzi ndi anthu a Mulungu, kuposa kuti akasangalale ndi zisangalatso za tchimo kwa kanthawi;

Anachiyesa chitonzo cha Khristu chuma chachikulu kuposa chuma cha ku Igupto: . . . ndipo anabwezedwa mphotho.

Mwa chikhulupiro anasiya Igupto, osawopa mkwiyo wa mfumu: pakuti iye anapirira molimbika, ngati kuti akumuwona iye amene ali mosawonekayo.

³⁴ Ine ndikufuna kuti nditenge phunziro, mmawa uno, “kusankha mwa chikhulupiro.” Ndipo ndikufuna kuti nditenge mwa mutu, mawu oyambirira atatu a mutu wa

23, “*Mwa Chikhulupiriro, Mose.*” Ndi, “kusankha mwa chikhulupiriro,” pafupifupi chirichonse chimene ife timachita, ife timayenera kuti tisankhe mwa chikhulupiriro. Ndipo zonse zimene ife tikumupeza kuti Mose anachita, zimene nzoyenera kuzibwereza, zinali mwa chikhulupiriro; osati mwa kupenya, koma mwa chikhulupiriro.

³⁵ Ndipo chifukwa chimene ine ndasankhira izi mmawa uno, kwa mpingo umene uli mu chikhulupiriro ichi, zakhala zakuti mu... ngakhale ma sukulu athu, ndi kozungulira, takhala tiri ndi kuphunzitsa kuchuluka kwa sayansi. Chifukwa cha izi, ife tawakokera anthu kutali ndi chikhulupiriro. Tsopano, chikhulupiriro sichimatsimikiziridwa ndi sayansi. Chikhulupiriro ndi chimene sayansi siimatha kuchiwona. Ndipo ife... Ngati ife titi tidzataye konse chikhulupiriro chachikulu ichi, ndiye kuti ife tidzakhala kwathunthu mu mdima, iwo... ziribe kanthu kaya ndife ophunzira bwino chotani, momwe ife tingakhoze kuwafotokozera Mawu a Mulungu, kuti azigwirizana ndi njira yathu ya kakhulupiridwe.

³⁶ Palibepo njira yomwe tingamusangalatsire konse Mulungu: ndi mwa chikhulupiriro basi. Lemba limanena izo mwachimvekere mwanjira imeneyo, ndipo izo zimakhala mwachikhulupiriro. “Ndipo popanda chikhulupiriro,” limatero Lemba, “ndi zosatheka kuti timukondweretse Mulungu.”

³⁷ Kotero, ngati chikhulupiriro chikutsutsana ndi sayansi, ndipo sayansi ikutsutsana ndi chikhulupiriro, zimenezo zimaziika izo mo—mokhulana kwa china ndi chimzake, ndiye ife tiyenera kuti tizitenga chisankho monga Mose anachitira. Mwa chikhulupiriro ife timakhulupirira!

³⁸ Tsopano, ngati ife titaya chikhulupiriro, ndiye kuti sitidzatha kuyankhidwa pemphero ndi Mulungu. “Pakuti iye amene abwera kwa Mulungu poyamba ayenera kukhulupirira kuti Iye ali, ndi wopereka mphotho kwa iwo amene akumufunafuna Iye mosamalitsa.” Kotero, ngati ife titaya chikhulupiriro, mapemphero athu amakhala opanda mphamvu; ife sitimafika kulikonse.

³⁹ Kotero ndizo zonse zomwe ife tingathe kuziganizira, mmawa uno, ndi kugwiritsitsa kwa chikhulupiriro. Ndiye, ngati ife titaya chikhulupiriro, chiyembekezero chathu chonse chimatayika. Ndipo ngati ife titaya chikhulupiriro, zenizeni zathu zonse zauzimu zitayika. Chifukwa, iwe sungathe kukhala ndi chikhulupiriro mu zinthu zomwe iwe ukuziwona, chifukwa zinthu zomwe iwe ukuziwona zonsezo ndi zakutha.

⁴⁰ Ngati ife tikuyang’ana pa munthu wina wopambana, mtumiki wamkulu, kapena gulu lalikulu, zonse izo zidzatha, tsikulina. Ndipo ngati tingayang’ane pa fuko lalikulu, kapena chida chachikulu, zonsezo zidzatha, tsikulina. Ndiyeno ife tiyenera kukhala mwa chikhulupiriro, kwa zinthu izo

zomwe sayansi siimazinena. Ndi mwa chikhulupiriro kuti ife timakhulupirira.

⁴¹ Tsopano, ife tingataye ulemerero wathu ngati ife titaya chikhulupiriro. Tsopano, ngati ife tichoka kwa chikhulupiriro, ndiye kuti ife tikuwutengera mpingo ku dera la zaluntha.

⁴² Ndipo nthawi zambiri, zakhala zikuganiziridwa, pakati pa anthu, kuti chifukwa chakuti gululo linali lalikulu, ndipo iwo anali ndi matchalitchi akuluakulu, zipilala zikuluzikulu, ndi aakulu, anthu ambiri ovala-bwino ndi okonzedwa, ndi ndalama zambiri, mwakuti iwo akhoza kukwanitsa chinthu chimenecho, ife, nthawi zambiri, tinkaganiza kuti zimenezo ndi zodzoza, kuti mpingo umenewu uyenera kuti ndi wodzozedwa. Kapena, ife kawirikawiri takhala tikulozera kwa azilaliki osiyana siyana amene amapita kumakalalikira uko ndi kumakakhala ndi osonkhana ochuluka a anthu, ndipo ife timaganiza, nthawizambiri, kuti iwowo ndi zizindikiro za kudzoza. Koma zimenezo sindizo palimodzi choonadi. Kumeneko ndi kudzoza kwa umunthu.

⁴³ Koma kudzoza kwenikweni kumabwera pa kuchita chifuniro cha Mulungu. Mukuona? Kaya ndi mmodzi, kapena ongokwanira mdzanja. Kaya ndi tchalitchi chachikulu, kapena tchalitchi chaching'ono, zimenezo ziribe ntchito. Kaya iyeyo ndi wodziwa kulankhula, wopambana, kapena wangokhala munthu wosadziwa nkomwe ABC yake, zimenezo ziribe ntchito. Izo zimatengera uthenga umene iyeyo akuubweretsa, ngati iwo uli wodzozedwa ndi Mawu a Mulungu.

⁴⁴ Kapena, kodi ndi wodzozedwa ndi kumvetisa kwaluntha kwa kudzoza kwa umunthu? Anthu ena akhoza kudzozedwa chifukwa cha wolankhula molakatula. Izo sizimapanga izo kukhala zolondola. Nthawizina iwo amakhala odzozedwa chifukwa chakuti munthuyo ndi wophunzitsidwa bwino kwambiri mwakuti iye akhoza kuloza mfundo yake. Zimenezo sizikutanthauza kuti ndi za Mulungu. Mukuona?

⁴⁵ Ndi kudzera mu Mawu a Mulungu okha a nthawizonse, odala Amuyaya, ndi momwe ife titha kulandira kudzoza, ndipo kumeneko kumaperekedwa ndi Mzimu Woyera. Mwa chikhulupiriro ife timalandira iko.

⁴⁶ Tsopano ife tikhoza kuganiza za Mose, ndi nthawi yopambana iyi ya moyo wake. Ndipo ife nkuwerenganso mmbuyo, za kubadwa kwake, mmene Mulungu anamusamalilira iye, koma apo panabwera nthawi mu moyo wa Mose imene pankayenera kuti pakhale nthawi yosankha. Ngati ife tingawerenge molondola, ife tikupeza kuti iye anali mwana wa mwana wamkazi wa Farao, ndipo anali woti adzakhale wolowa mpando wachifumu, ndipo akanadzakhala farao wotsatira mu Igupto. Kotero iye amatha kuzindikira akamayang'anayang'ana, atafika pokula ndi pozindikira, ndipo apo pamakhoza kukhala

akapolo amenewo akugwira ntchito mmaenje a matope. Ndipo Mose, pamene iye ankayang'ana kudzera mmazenera a nyumba yachifumu, pa akapolo omwewo amene Farao ankawayang'ana, koma panali kusiyana bwanji mmayang'anidwewo.

47 Ine ndikufuna kuti ndikhazikitse lingaliro limenelo, mmawa uno, kwa maminiti pang'ono, ndipo Mulungu wa Kumwamba atazifikitsa izo mkati kwa mtima uliwonse pano. Ndi mmene iwe umayang'anira pa china chirichonse, ndi chimene chimapangitsa kusiyanitsa.

48 Mvangeliki wamkulu, John Sprawl, amene anali wotembenezidwa ndi utumiki wa M'bale Bosworth, amene ambiri a inu mukumukumbukira zaka zambiri zapitazo, wa ku Old Glory Barn. Iye anati, tsiku lina anali paulendo, asanamwalire bwenzi ndi mkazi wake wokondedwa. Iwo anali ku La Salle Lorraines, ku France. Ndipo ine ndinali nawo mwayi wokafika ku malo omwewo. Ndipo namulondola anali kuwayendetsa iwo kudutsa mmindayo, ndi kumawawonetsa iwo zinthu zosiyanasiyana. Ndipo iwo anafika pa chosemedwa china cha Ambuye Yesu, mtanda. Ndipo Bambo Sprawl anali atayima pambali, akuyang'ana pa icho, iye ndi mkazi wake, ndipo, mmitima mwawo, anali akutsutsa chomwe walusoyo anali nacho mmalingaliro, kapena wosemayo, kani, pamene iye ankasema kuchokera mmwala, chinthu chowoneka moyipa icho kuti chikakhale chikuimira mazunzo ndi chikondi ndi chisoni cha Ambuye Yesu, ndi mmene chinkawonekera moyipa ndi chogobedwa. Ndipo namulondolayo anabwera kwa Bambo Sprawl, ndipo iye anati, "Bwana, ine ndikuwona kuti inu mukuchitsutsa chosemedwa ichi cha Ambuye Yesu."

Ndipo iye anati, "Ine ndikutero."

49 Ndipo iye anati, "Ine sindikudamwa nkomwe, chifukwa anthu ambiri amene amayang'ana pa icho, koyamba, iwo amachitsutsa icho."

50 Ndipo Bambo Sprawl anati, "Bwanji, ine sindikuwonapo chisoni chirichonse kapena kuzodza kulikonse poyang'ana pa chinthu chimenecho, kotero ndikudadwa chifukwa chimene wosemayo anachipanga icho monga chonchi."

51 "Ndipo wosemayo . . ." Anati, "Bambo Sprawl, chosemedwa ichi ndi chabwinobwino, ndipo wosemayo anali nacho chinthu cholondola mmalingaliro mwake. Koma pamene pali vuto, ndi inuyo. Ndi mmene inu mukuyang'anira pa icho." Ndipo anamugwira mkazi wake pa dzanja, ndipo anapita naye iye pa guwa pa phazi pa mtanda umenewu. Ndipo iye anati, "Tsopano, Bambo Sprawl, tayang'anani mmwamba tsopano." Ndipo pamene anayang'ana mmwamba, iye anati mtima wake unakhala ngati ukuchokamo. Zinali zosiyana bwanji, kukaima pambali ndi kukachiyang'ana icho mwanjira *imeneyo*, ndi

kupita pansi ndi kukachiyang'ana icho mwanjira yomwe chinapangidwa kuti chiziyang'anidwira.

⁵² Ndipo umo ndi mmene Mulungu aliri. Umo ndi mmene chikhulupiro chiliri. Ndi mmene iwe umayang'anira pa icho. Ngati iwe uyang'ana pa ilo ngati Baibulo lina la mbiriyakale, la chinachake chimene chinalipo mmasiku amene anadutsa, iwe sudzatha konse kuti upeze phindu lenileni la Baibulo. Iwe umayenera kuti ugwade pa maondo ako, ndi kumamvera malamulo a Baibulo ili, ndi kuyang'ana pa Ilo podzera mmaso a Mzimu Woyera.

⁵³ Ine ndingafunse omvetsera awa, mmawa uno. Ndi ubwino wanji umene Mulungu wa mbiriyakale angatichitire ife lero ngati Iye siali Mulungu yemwe yemweyo? Ndi chabwino chanji chimene Mulungu, amene angamutenge Mose ndi kupanga naye iye zozizwitsa zomwe iye anachita, ndi chaubwino wanji kwa ife kuti tiwerenge za Mulungu ameneyo ngati Iye sangakhale Yemweyo lero? Angakhale wabwino bwanji Mulungu amene angapululumutse kuchokera mng'anjo ya moto, ana a Chiheberi, ngati Iye siali Mulungu yemwe yemweyo lero? Angakhale wabwino bwanji Mulungu yemwe ankaweruzza pakati pa chabwino ndi choyipa, mu tsiku lammbuyomu, ndi kuwalanga olakwa ndi kudalitsa abwino, ngati Iye sangakhale Mulungu yemwe yemweyo lero? Kodi ife timapitiranji ku tchalitchi? Ndi chifukwa chiyani ife timazipewa zinthu za mdziko, ngati Iye siali Mulungu yemwe yemweyo wa chiweruzo chomwecho, ndi lingaliro lomwe lomwelo limene Iye amakhala nalo nthawizonse? Angakhale ndi ubwino wanji Mulungu amene angakhudze dzanja la mzimayi wa malungo, ndipo malungowo ndi kutha, ngati Iye sakhala Mulungu yemwe yemweyo lero? Chingakhale ndi ubwino wanji kumutumikira Mulungu amene anamuitana nzake kuchokera mmanda, atafa kwa masiku anai, ngati Iye sangakhale Mulungu yemwe yemweyo lero?

⁵⁴ Mwa chikhulupiro ife tikukhulupirira, kuti, tsiku lina la ulemerero Iye adzatiitana ife kuchokera pa dziko lapansi, ngakhale ife titakhala ka supuni ka phulusa panonso. Kodi ife timatsimikizira chotani zimenezo? Ife sitimatsimikizira izo. Ife timakhulupirira izo. Ife sitimafunsidwa kuti tizitsimikizira chirichonse. Ife timafunsidwa kuti tizikhulupirira izo.

⁵⁵ Mwa chikhulupiro Mose anachita *zakuti-ndi-zakuti*. Ndipo monga Mose, ngati mnyamata, anayang'ana kudzera pa zenera la nyumba yachifumu, pa akapolo, iye anawona gulu lomwelo la akapolo, amatope, otuwa, okhala ndi matope omwe Farao ankawawona.

⁵⁶ Ndipo pamene Farao ankayang'ana pa iwo, ndi Aigupto, iwo sanali kanthu koma gulu la akapolo. Ndicho chimene iwo ankakhalira abwino; kungokhala anthu oponda matope, kuti azipanga njerwa zadothi kwa ubwino wa mizinda yomwe

Farao anali kumanga. Umo ndi mmene Aigupto ndi Farao ankayang'anira pa akapolo.

⁵⁷ Koma Mose, pamene iye ankayang'ana pa iwo, anali mayang'anidwe osiyana omwe Mose anali nawo. Pamene iye ankawona, akamadutsa pa zenera, makwinya aakulu pankhope zawo, misonzi yomwe inkatsikira pansu mmatsaya mwawo, ndi matupi awo opindika, iye ankayang'ana pa iwo ngati anthu a Mulungu. Iye sankayang'ana pa iwo ngati akapolo. Iye ankayang'ana pa iwo ngati anthu osankhidwa a Mulungu.

⁵⁸ Ndipo, o, pamene ine ndikuyenda, dziko ndi dziko, ndi fuko ndi fuko, kulalikirira! Pamene ine ndinachoka pa zitseko za kachisi wamng'ono uyu, awo ndi malo a zipembedzo zonse, opanda lamulo, koma chikondi, opanda bukhu koma Baibulo, ndi opanda kachikhulupiriro koma Khristu, ine ndayesera kuti ndiziyang'ana pa ana a Mulungu, ndi pa okanidwawo, kuti ndiwo anthu osankhika ndi oitanidwa a Mulungu. Ine sindimawafunsa iwo ngati iwo ali aku Branham Tabernacle. Ine sindimawafunsa iwo ngati iwo ali a Methodisti, kapena ngati iwo ali a Presbateria, kapena ngati iwo ali Achipentekoste, kapena Anazareni, kapena a Pilgrim Holiness. Ine ndimangofuna kuti ndiziyang'ana pa iwo ngati anthu a Mulungu. Ndi kumawona zochita zawo ndi kachitidwe kawo, kuti iwowo ndi antchito a Ambuye Mulungu. Ndipo mtima wanga umakhumba chiyanjano ndi iwo, ziribe kanthu kuti iwowo ndi a dzina lanji. Ine ndimangofuna chiyanjano chawo. Ine ndimawakonda iwo chifukwa ine ndimadziwa iwowo ndi anthu a Mulungu.

⁵⁹ Pamene ine ndimuwona mkazi akubwera mu msewu, ali ndi siketi yaitali, ndi tsitsi lake atalikonza bwino kumbuyo, ndi—ndipo atavala—diresi yowoneka bwino; ndipo ine nkumuwona dona wina wamng'ono, mwinamwake wausinkhu wofanana, atavala kabudula wamng'ono; iye akhoza kukhala, mmawonekedwe, wokongola pawiri kumuposa mkazi wa tsitsi lalitali uja, monga mwa mwamayang'anidwe a dziko lapansi, koma ine ndingatenge mbali yanga ndi mtsikana uyo amene wavala ngati Mkhristu. Ngakhale iwo atamamuseka iye, ndi kumamutcha iye wotengeka, komabe, ine ndingatenge mbali yanga. Iye akhoza kusakhala wokongola monga mtsikana winayo, mwamawonekedwe, koma iye akumawona chinachake. Mwa chikhulupiriro iye akumamuwona Iye Amene ali wosawonekayo, Amene akutsogolera moyo wake.

⁶⁰ Pamene ine ndimuwona mwamuna ali pa ntchito, akutchedwa “dikoni,” kapena “mlaliki,” kapena “wotengeka,” chifukwa iye amakana kusuta, ndi kumwa mowa, ndi kumapita ku dansi, monga ena onse a iwo, ndipo iye nkumatchedwa “wotengeka,” mtima wanga umapita kwa iye. Iyeyo ndi m'bale wanga, kuno mu mchenga wa Igupto uwu, zimenezo zimapangitsa mtima wathu kumalalakala kuti timukumbatire

iyе ndikuti, “M’bale, ife ndi ammwendamnjira ndi alendo, a dziko lino, ndipo ine ndikulakalaka kuti ndiziyanjana ndi inu.”

Mose anachita kupanga chisankho, kusankha mwa chikhulupiriro.

⁶¹ Ndi anyamata angati amene akadalumphirapo pa mwayi uwu wokhala mwana wa mwamuna wa mwana wamkazi wa Farao! Ndi anyamata angati amene akadalumphirapo pa mwayi uwo umene Mose anali nawo, kuti akasangalale nazo zokondweretsa ndi zokoma zonse za pa dziko lapansi, kuti adzakhale mfumu yaku Igupto, kuti akakhale nalo dziko lonse pa mapazi ake! “Ndi chinthu chopusa bwanji,” anyamata a tsiku lake ayenera kuti anaganizirapo, “pamene Mose anasankha kuti akatenge malo ake ndi anthu osautsika ndi ozunzidwa a Mulungu.”

⁶² Nchifukwa chiyani iye anachita zimenezo? Mwa chikhulupiriro, pamene iye anakwezera mmwamba maso ake, iye anayang’ana kudutsa zonyezimira zonse za dziko lino. Iye anayang’ana kudutsa zosangalatsa za tchimo. Ndipo Baibulo limanena kuti iye anapirira pomuwona Iye Amene anali wosawonekayo, mwa chikhulupiriro, ndipo anapanga chisankho choti azimutumikira Mulungu ameneyo mosasamala zomwe zinachitika.

⁶³ Izo sizinasinthe ayi. Ambiri a ife tikhoza kumapita kumene ife tingakutche kuti ndi nyumba yabwinoko. Ife tikhoza kumakasangalalako, mwinamwake, ndi chiyanjano ndi kukoma kokhala pa mpando wabwinoko. Ife tikhoza kukhala otchuka kwambiri, kumakamwa ndi kumakasuta, ndi kumakavala ndi kumakachita monga dziko lapansi. Koma vuto lake ndi chiyani? Inu mwakwezera mmwamba maso anu, ndipo mwachikhulupiriro inu mukumuwona Iye Amene ali wosawonekayo, ndipo mwatenga maimidwe anu ndi okanidwa ndi otchedwa ojera-odzigudubuza a tsikuli. Pakuti mwa chikhulupiriro ife tikumuwona Iye Amene ali wosawonekayo, kusankha kuzunzika mazunzo ndi msautso.

⁶⁴ Ine sindinganene kwa anthu kuti asankhe kuti azizunzidwa. Ine sindikunena kuti inu musankhe kuzunzidwa. Ichо sichingakhale chinthu cha umunthu kuti ndichite zimenezo. Koma ngati kuzunzikako kuli pa njira ya ntchito, ndiye tiyeni tizitenge izo momwe izo zikubwerera. Ine sindikufuna kuti inu mumuchitire chinachake munthu winawake kuti azikusekani inu. Ine sindingafune kuti inu muzinena zinthu zosiyana, zimene ine... “Ine ndi wa mpingo umene sumakhulupirira *zakuti-ndi-zakuti*, mu dziko la dziko lapansi,” ndi zinthu monga choncho, basi kuti anthu azikusekani inu. Inu mukuzibweretsera zimenezo pa inueni. Ine sindinganene kuti inu mutuluke kuno ndi kumakapitirira ndi kumakachita chinachake chimene chiri chosokoneza. Ine sindingafune kuti inu muzikachita

zimenezo, kuti wina azikanena kuti ndinu wotengeka. Inu mukuzibweretsera zimenezo pa inueni. Koma ngati izo ziri mu njira yanu ya ntchito kwa Mulungu, musiyeye dziko linene zomwe iwo akufuna kuti anene. Inu zikhalanibe moyo.

Iwe umapanga chisankho. Mwamuna aliyense ndi mkazi ayenera kupanga zimenezi.

⁶⁵ Nanga bwanji ngati Farao akanawona zomwe Mose ankawona? Iye ankawona kuzunzika kwa anthu. Iye ankadziwa mtengo umene ankayenera kulipira. Koma mwachikhulupiriro iye anasankha zimenezo, kusiyana ndi kuti azikakhala ndi zosangalatsa za tchimo.

⁶⁶ Alipo mwinamwake atsikana aang’ono, achichepere akhala apa, monga atsikana okongola aang’ono. Dziko likanakonda litanena kwa inu, “Chita *ichi-ndi-icho*. Iwe ndi wokongola. Thupi lako linawumbidwa mokongola kwambiri. Iwe uziwonetsa zimenezo.”

⁶⁷ Koma, mlongo wanga, kweza maso ako mmwamba ndipo uyang’ane kupitirira zimenezo, kwa Iye amene anati, “Ndi chonyansa kuti mkazi avale chovala cha mwamuna.”

⁶⁸ Ngati amuna a anthu a mu dera lanulo, ngati akazi omwe inu mumayanjana nawo, akuti, “Dulani tsitsi lalitali ilo. Muziwoneka bwino. Zikhala *ichi, icho*, kapena *chinacho*. Kapena, Izo zikupangitsa iwe kuwonekako bwino.” Iwe usamvetsere kwa zimenezo!

⁶⁹ Iwe ukwezere mmwamba maso ako, ndipo mwa chikhulupiriro umuwona Iye amene anati, “Tsitsi la mkazi ndi ulemerero wake, ndipo iye asamalidule ilo.”

⁷⁰ Ngati iwo anena kuti, “Zikhala zotchuka. Iwe zikuyendera bwino ku ntchito yako, kapena ndi abwana ako, ngati iwe utamwa chakumwa choledzeretsa. Ngati iwe utasuta ndudu monga akazi ena onse, iwe ungamakhale mosangalala mwa oyandikana nawo ako.”

⁷¹ Mwa chikhulupiriro uzikwezera maso ako ndi kuyang’ana kwa Iye Amene anati, “Detsani thupi ili, ndipo Ine ndidzaliwononga ilo.” Mwa chikhulupiriro ife timazikhulupirira zinthu zimenezo. Si zimene inu mwaziwona. Ndi chinachake chimene iwe umachikhulupirira. Mwa chikhulupiriro, Mose anatero.

⁷² Ndipo mu kuyenda kwa chikhulupiriro uku, pamafika nthawi imene pamayenera kukhala kusankha.

⁷³ Loti anapanga kulakwitsa komvetsa chisoni uko kumene ife timapanga. Nthawi zambiri ife timasankha kwa ubwino wathu wathu. Ife timasankha zinthu zomwe zingakhale zabwinoko.

⁷⁴ Nthawizina ngati pali makangano pang’ono amene abwera mu tchalitchi, ndipo winawake nkuti, “Chabwino, adikoni kapena abusa ali kumbali iyi.” Musayang’ane pa zimenezo.

Muziyang'ana pa chomwe chiri cholungama. Muchichotsepo chinthu chimenecho ndipo muwabweretsepo onsewo palimodzi. Zimenezo ndi zaumulungu.

⁷⁵ Kulipo kusankha. Ndipo ife timazisankhira tokha. Ife timasankha chinachake chimene chiri cha kwa ubwino wathu.

⁷⁶ Koma Mose anasankha zosautsa ndi chitonzo, kuti akathe kuyenda ndi anthu a Mulungu. Taganizani za zimenezo tsopano. Tamvetserani kwa izo. “Anasankha zosautsa za anthu a Mulungu, ndipo anachiyesa icho chuma chopambana, pakuti iye anapirira, pomuwona Iye Amene anali wosawonekayo.”

Tsopano, Loti, nthawi ina, anayenera kupanga chisankho.

⁷⁷ Ndipo izo zikhoza kukhala, mmawa uno, kuti pakhala amuna ndi akazi amene akhala pano, amene muti mupange chisankho chanu chomaliza. Inu muli lero chomwe inu muli, chifukwa zaka zingapo zapitazo inu munasankha kuti mudzakhale chimene inu muli tsopano. Ndipo chimene inu muti musankhe tsopano chidzanena chimene inu muti mudzakhale zaka zisanu kuchokera pano. Zaka zisanu kuchokera lero mukhoza kudzakhala wa misionare. Zaka zisanu kuchokera pano mukhoza kudzakhala Mkristu wodziwika.

⁷⁸ Kapena, zaka zisanu kuchokera pano mukhoza kudzakhala ku gehena, chifukwa inu munapanga chisankho cholakwika. Zaka zisanu kuchokera lero mukhoza kudzakhala mukupukuta masanzi mu chipinda cha bala. Zaka zisanu kuchokera pano inu mukhoza kudzakhala hule la pa msewu.

⁷⁹ Kapena, inu mukhoza kudzakhala mwamuna kapena mkazi yemwe—angakhale waphindu kwa anthu ena ali onse, chifukwa choti munasankha Khristu. Zaka zisanu kuchokera pano mukhoza kudzakhala muli ku Ulemerero, mutapita mu Mkwatulo, chifukwa inu mwapanga chisankho chanu lero.

⁸⁰ Koma inu muyenera kusankha. Ndipo musamayang'ane pa zimene inu mukuziwona. Muzisankha zimene inu mukuziwona mwa chikhulupiriro. Ndi chinthu chokhacho chomwe chiti chidzawerengedwe, ndi chimene—chimene inu mwasankha mwa chikhulupiriro.

⁸¹ Loti, monga mmene iye ankayenera kuti apangire chisankho. Abrahamu anamupatsa Loti chisankho chake.

⁸² Ndipo Mulungu akukupatsani inu chisankho chanu. “Musankhe inu lero kuti mutumikira ndani.” Mmunda wa Edeni munali mtengo wa—wa chidziwitso, ndi Mtengo wa Moyo. Munthu anapatsidwa mwayi kuti asankhe umene iye ankaufuna. Ndipo ziri chomwechonso lero. Inu mwapatsidwa mwayi wanu, ngati anthu ochita mwakufuna kwawo, kuti muzisankha chirichonse chimene inu mukufuna kuti musankhe.

⁸³ Langizo langa kwa inu, ndilo, musamayang'ane pa zinthu zamakono zomwe zakuzungulirani inu, ndi kutchuka ndi

kukongola komwe inu mungathe kukhala. Koma muzisankha, kani, mwa chikhulupiriro, Iye amene anapereka lonjezo kuti tsiku lina Iye adzabwera ndipo adzakonza zolakwika zonse, ndipo adzakupatsani inu Moyo Wamuyaya, ndipo adzakuwukitsani inu. Ziribe kanthu ngati inu mutatenga njira yonyozeka ndi apang’ono a Ambuye, mupange chisankho chimenecho. Ngati muli mavuto mdzanja, ngati muli mavuto mdziko, ngati muli mavuto mu tchalitchi, ngati pali mavuto pakhomo, ziribe kanthu kuti ziri kuti, mupange chisankho chanu, “Mwa chikhulupiriro, ine ndimutumikira Mulungu. Ine ndiwuchepetsa mtima wanga mu Kukhalapo Kwake. Ine nditenga njira ndi ana a Mulungu. Ine ndiziwawona iwo akunyozedwa ndi kukanidwa, ndi kuthamangitsidwa ndi kusekedwa, koma ine ndizitengabe malo anga a ntchito. Ine ndizikhalabe pomwepo. Ndipo pamene iwo akulira, ine ndizilira nawo limodzi. Ndipo pamene pali chisoni, ine ndidzakhala nawo limodzi pa chisonicho. Momwe iwo azikhalira moyo, inenso ndidzikhala momwemo.”

⁸⁴ Monga Naomi ananena...Kapena, Rute ananena kwa Naomi, “Njira zanu zikakhala njira zanga. Njira zanga zikakhala njira zanu. Komwe muti mukakhale, ine ndikakhalako. Komwe inu mukupita, ine ndidzapitako. Mulungu yemwe inu mukutumikira adzakakhala Mulungu wanga.” Mutenge chisankho chimenecho, ngakhale zitasupula mnofu kumene wa chikumbumtima chanu, cha kumaganiza kuti ndinu winawake. Mudzivule nokha khungulo ndipo mutenge njira yanu ndi onyozeka apang’ono a Ambuye, ndi kukhala wokhulupirika ku malo a utumiki ndi pa malo a ntchito.

⁸⁵ Loti anayang’ana pozungulira. Iye anati, “Ine ndiri ndi chisankho.” Ndipo iye anayang’ana chaku Sodomu. Iye anawona minda yabwino ya msipu yomwe inali yabwino kusiyana ndi yomwe Abrahamu anaiwona, ndi kumene kunali Abrahamu. Iye anawona mwayi woti azikadyetserako ziweto zake, kuti akakhale ndi ng’ombe zonenepa ndi zabwino.

⁸⁶ Ine ndikuyembekeza kuti ine sindikupweteka kumverera kwa aliyense. Koma awo akhala maimidwe a azilaliki ambiri, kumanyengerera Uthenga, kumaganiza kuti apeza ndalama zambiri akamachita zimenezo. [M’bale Branham akuwomba mmanja mwake katatu—Mkonzi.] Chitupa chodyera! Ine bola ndizikakhala mu dziko losabala, nkumakadya, kumakamwa kuchokera mngalande, ndi kumakadyako zikondamoyo, kusiyana ndikuti ndizinyengerera pa kumverera kwa chikhulupiriro changa mu Mawu a Mulungu a Moyo. Ine nditenga njira yanga.

⁸⁷ Ena a iwo anati, “Billy, chavuta ndi chiani ndi msonkhano wako, pakuti kukumakhala Achipentekoste ochuluka kwambiri pa iyo.” Mtumiki wamkulu wa chipembedzo ananena zimenezo.

Ine ndinati, “Kodi chipembedzo chanu chizithandizira msonkhano wanga?”

⁸⁸ Osati kale litali, mu *Look* magazine, ine ndikukhulupirira, munali nkhani. Ndipo wolembayo ananena mmenemo, amakamba za anthu Achipentekoste. Iye anati, “Mpingo wa Chipentekoste ndi mpingo umene ukukula kwambiri mdziko lero.” Chifukwa chiyani? Ndi chifukwa chakuti amuna ndi akazi akwezera maso awo mmwamba ndipo akuyang’ana kutali.

⁸⁹ Ndipo mlembiyo anawayamikiranso anthu Achipentekoste. O, zoon, iye anati, “Analipo ena a iwo omwe ankachita mosokoneza, ndi zina zotero. Koma, a Methodisti amapembedza kachikhulupiriro. Iwo amapembedza Mulungu mwa kachikhulupiriro. Achibaptisti amachita chimodzimodzi, ndi Achipresbateria. Koma Achipentekoste amapembedza ndi Baibulo lake.”

⁹⁰ Mwa chikhulupiriro ife tikuwona lonjezo. Ine nditenga gawo langa ndi iwo, ziribe kanthu kuti iwowo akunyozedwa mochulukwa bwanji, ine ndikadali mmodzi wa iwo. Ngakhale iwo azisekedwa, ndipo nkumakhala ndi zokhoza ndi zolephera zawo, monga Israeli ankachitira, ine sindingafune kuti ndiime ndi mneneri wabodza kumbali ya phiri, Balaamu, ndi kuyesera kuti nditemberere chimene Mulungu wachidalitsa. Chifukwa, mu msasa umenewo munali Thanthwe lokanthidwa, ndi Nsembe ya magazi, ndi Lawi la Moto. Zinalibe kanthu kuti iwowo ndi chiyani, izo zikuwatsogolera iwo mpaka ku chigonjetso, ndipo iwo ayenera kufika kwa icho, chifukwa iwowo ndi anthu olonjezedwa amene akuyenda mwa chikhulupiriro. Ngakhale iwo asakhale achipembedzo, iwo anali ongyendayenda, ndipo ndi momwe amakhalira anthu a Mulungu. Koma ine ndikufuna kuti nditenge njira yanga ndi iwo, kugwirana nawo iwo mmaimidwe awo; osati mu chipembedzo chawo, koma mu chiyanjano chawo pozungulira zinthu za Mzimu Wamuyaya wa Mulungu, chimene, mwa chikhulupiriro ine ndinalandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Mulungu andithandize ine kuti nthawizonse ndizikhala nako kachitidwe kameneko.

⁹¹ Zindikirani. Pamene iwo anali kupita patsogolo, ife tikupeza kuti Loti anawona mwayi wa—wa ng’ombe yonenepa. Ambiri amawona mwayi wa thumba la ndalama lonenepa. Ambiri amawona mwayi wa kuchita bwino. Iye anawona kuthekera kokhala ndi madola ochulukirapo. Iye anawona kuthekera kokhala meya wa mzinda. Pokhala mlendo, ndi munthu wa nzeru, yemwe iye anali, “Mwina ine ndidzakhala mfumu ya mzinda.” Iye anawona kuthekera chifukwa izo zinali zili patsogolo pake. Koma iye sanawuwone moto umene unali woti udzawononga dzikolo. Iye sanalingalire payekha, kuti dzikolo linali lodzadza ndi tchimo, ndipo Mulungu anachita kuliwononga ilo.

92 Ndipo, lero, anthu akumayesera kuti azizilimbikitsa okha pomanena kuti, “Kodi ndinu. . .”

Ine ndikati, “Kodi ndinu Mkhristu?”

93 Iwo amati, “Ndine wa Chimereka.” Zimenezo ziribenso kanthu kochita ndi izo kuposa kuyesera kumuuza khwangwala kuti iye ndi chule. Izo ziribe kanthu kochita ndi zimenezo. [M’bale Branham akuwomba mmanja mwake kamodzi—Mkonzi.]

94 Iye adzawonongedwa, chifukwa Mulungu ndi wolungama. Ndipo ngati Amerika angamapitirire ndi machimo ake, Mulungu wolungama ndi wochita mwayekha, woyera adzakhala wokakamizidwa ku—kuti akadzutse Sodomu ndi Gomora ndi kukapepesa kwa iwo chifukwa chowaotcha iwo, chifukwa cha tchimo lawo; ngati Iye angatilole ife kuti tizipitirira nazo.

95 Ngati Iye angadzakuloleni inu kuti mukafike Kumwamba ndi ntchito zanu zosalungamazo, Iye adzayenera kuti adzamudzutse Anania ndi Safira ndi kudzawapatsanso iwo mwayi wina. Iye ndithudi angadzatero. Koma Iye ndi wolungama. Anania anawona ndalama zake. Petro anamuwona Khristu.

96 O, mai! Loti sanawone kuwonongeka kwa ana ake ku malo amenewo.

97 Ambiri a inu, lero, mwagwira pozungulira tizikhulupiriro takale tofunda iti ndi zinthu, inu simukuwona kupulikira kwa ana ndi kuwonongedwa kwa ana anu. Inu simumamuwona mwana wanu wamkazi ali mu nyumba ya chiwerewere. Inu simumamuwona mwana wanu wamwamuna ali chidakhwa, kapena ali pa tebulo la njuga kwina kwake.

98 “Chifukwa iye amathiriridwa bwino-madzi.” Ndipo tchimo silimakhudzidwa. Iye sanamuwone mkazi wake, mutu wa mabungwe onse, akusanduka chulu cha mchere, pamene iye anali kuyang’ana. Iye sanamuwone iye akuthawa atatsala pang’ono kuti alumidwe ndi mano ake, akupita ku mzinda wawung’ono kwina kwake, akuthawitsa moyo wake. Iye sanawone zimenezo, chifukwa iye ankangoyang’ana zokhazo zimene iye ankaziwona patsogolo pake.

99 Koma, Abrahamu, iye sankaliwona dziko lothiriridwa bwino-madzilo, pakuti iye anakwezera maso ake mmwamba ndipo anawona za mawa, pakuti iye akanadzalandira zinthu zonse. Mkhristu weniweni lero amakwezera maso ake mmwamba ndipo amawona lonjezo la Khristu. “Odala ndi ofatsa pakuti iwo adzalandira zinthu zonse. Iwo adzalandira dziko lapansi.” Mkhristu weniweni, mwa chikhulupiriro, amayang’ana mmwamba ndipo amawona zimenezo. Mutchuleni iye chimene inu mukuchifuna. Iye anakweza mmwamba maso ake. Ndipo pamene iye anachita zimenezo, Mulungu anati,

“Abrahamu, yenda kudutsa mdzikoli, lonsele ndi lako.” Mwa chikhulupiriro, Abrahamu anachita zimenezo; chikhulupiriro chomwe chomwecho chimene Mose anali nacho.

¹⁰⁰ Zinalembedwapo ndi wochitira ndemanga wina, amene ananena izi. Ine ndinkaganiza kuti awo anali mawu okongola kwambiri. Kuti Abra- . . . “Mose anatenga zokoma za mdziko ndipo anaziyika kumbali imodzi ya muyezo; ndi zoipisitsa za chipembedzo, ndipo anakaziyika izo kumbali ya muyezowo; ndipo za chipembedzo zinalamera kuposa zokoma za mdziko.”

¹⁰¹ Ziri chimodzimodzinso lero, kuti ngati ife titatchedwa chirichonse chimene ife tikufuna kuti tikatchedwe, “otengeka,” kapena “achiritsi Auzimu,” kapena “oyera-odzigudubuza,” kapena chirichonse chimene iwo akufuna kutitchula. Choipisitsa chimene ife tiri chidzalemera kuposa chopambana chimene dziko lingakwanitse. Iwo amafuna kuti adzitchedwa “otengeka akachitidwe-kachikale, okhuthala achikale.” Zimenezo zidzalemera kuposa chinthu chopambana chimene mdierekezi angati apereke kwa inu. Ndithudi izo zidzatero.

¹⁰² Mose anakweza chitonzo cha Khristu. Iye anamuwoneratu Khristu. Mtsogolo iye anadzalankhula mawu ena odzodza okhudza Iye. “Taonani, Ambuye Mulungu wanu adzazutsa mneneri wonga ine.” Iye ankadziwa. Iye anamuwoneratu Iye, ndipo anachiyesa chitonzo Chake chuma chopambana kuposa zokongola zonse za m’dziko.

¹⁰³ Mzanga wa Chikhristu, lero, kodi iwe sungachite zimenezo? Ndi kukongola konse ndi kutchuka kwa dziko, mwa chikhulupiriro, ife tikumuwona Iye amene analonjeza. Ndipo choipisitsa cha mpingo lero, mu chikhulupiriro chake chonsecho, komabe Izo zidzalemera kuposa chirichonse chimene mdierekezi angathe kukupatsani inu. Ngati ife tang’ambidwa, ngati ife tisweka mzidutswa, ngati ife tasokonezeka ndi kusweka, mu zipembedzo ndi zotengeka, izo zidzalemera kuposa chirichonse chimene mdierekezi angathe kukupatsani inu. Ndithudi.

¹⁰⁴ Iye anachiyesa chitonzo cha Khristu kukhala chuma chopambana kuposa chuma chonse cha Igupto. Ndiye iye anachita chinachake. Iye anasiya Igupto. O, ine ndimawakonda mawu amenewo. Iye anasiya Igupto. Mukuwona, iye anali akuyang’ana kudzera pa zenera lomwelo, koma iye anali akuyang’ana mosiyana ndi Farao. Nanga bwanji ngati Farao akanatha kuwawona mapeto ake? Bwanji ngati Farao akanawona fuko lake likumizidwa? Mose anaziwona izo. Motani? Mwa sayansi? Mwa chikhulupiriro, Mose anaziwona izo. Chirichonse chimene iye ankachita chinali mwa chikhulupiriro, chifukwa Mulungu anamulonjeza Abrahamu, atate ake, kuti Iye akanadza—Iye akanadzachezera fuko ili pakadzatha zaka foro handiredi, ndipo akanadzawatulutsanso iwo. Ndipo mwa chikhulupiriro, Mose anakhulupirira Mawu amene Mulungu

ananena, ndipo anazidziwa yekha, kuti ndi mwa chikhulupiriro, kuti anali mtsogoleri wosankhidwa kuti awatulutseko iwo. Iye ankadziwa kumene iye anali. Iye anatenga malo ake mmaenje a matope, ngati woponda matope, ndipo anachiyesa chitonzo cha Khristu chuma chopambana kuposa kuti akakhale pa mpando wachifumu wa Igupto. Iye anatenga. . . Iye sananene konse, “Ine ndikumva nazo chisoni izi.” Iye anatenga malo awo ndipo anapita limodzi nawo iwo! Ulemerero kwa. . . Iye anatenga malo awo. Ife tinapita limodzi nawo iwo.

¹⁰⁵ Nzosadabwitsa wolemba wodzozedwa anati:

Ine nditenga njira ndi onyozeka apang’ono a
Ambuye.
Ine ndayamba ndi Yesu, tsopano ine
ndikupyolatu.
Ine ndiri pa njira waku dziko la Kenani.
(Ndithudi.)

¹⁰⁶ Mose. Zinanenedwapo ndi wina kuti Mose anasankha, pamene iye akanakhala mwana wa Farao ndipo anali ndi zokongola za m’dziko, iye anasankha kuti akakhale mwana wa Abrahamu kuposa kuti akakhale mwana wa Farao. Mwana wa Abrahamu, wonyozekayo, kuposa kuti akakhale mwana wa Farao, mfumuyo.

¹⁰⁷ Ine kuli bwino ndikhale mwana wa Ambuye Yesu, ndi wantchito limodzi Wake, ndi kutenga malo anga limodzi ndi anthu okanidwa a dziko lino, kusiyana ndi kukakhala Purezidenti wa United States of America wamkulu uyu, kapena kukakhala Elvis Presley, kapena Pat Boone, kapena aliyense amene inu mukufuna kuti akhale. Ine nditenga njira yanga.

¹⁰⁸ Atsikana achichepere ayenera kuti atenge njira yawo. Mmalo momakhala a—Mary Pickfold, kapena katswiri wina wa pa kanema, mtsikana wina wokongola, mutenge njira yanu ndi onyozeka apang’ono a Ambuye.

¹⁰⁹ Ine bola ndikhale mlaliki pa gome, ndikulalikira chuma chosafufuzidwa cha Khristu, kusiyana kuti ndikakhale katswiri wa pa kanema waku Hollywood, kapena munthu wopambana kwambiri pa dziko lapansi. Ngati zinganditengere kumadya moperewera, kumapemphetsa, kapena chirichonse chimene ndingamachite. Ine ndidzatenga njira yanga ndi anthu a Ambuye. Mwa chikhulupiriro, ine ndidzachita zimenezo. Ine ndapatsidwapo mwayi. Koma, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndikuwonabe mwa chikhulupiriro.

Mwachikhulupiriro ine ndikuliwona ilo patali;
Ndipo Atate athu akudikirira panjira.
Kuti akatikonzere malo okakhalako
Kumeneko.

110 Munthu wa msonkho ananena, tsiku lina “Ndi chifukwa chiyani inu munaipereka nyumba yanu ku tchalitchi chija? Ndi chiyani chinakupangitsani inu kuti mupereke nyumba ya madola twente-faivi sauzande kwa kachisi wowoneka moyipa uja?”

111 Ine ndinati, “Sindinachitire izo tchalitchi. Ndi anthu amene ali mmenemo.” Ine ndiribe kalikonse ka katundu wa dziko lino. Tambala iliyonse ya ndalama yomwe ine ndimaipeza imapita ku tchalitchi ichi. Chifukwa chiyani? Chikhulupiriro changa chiri pa Mulungu, ndipo osati pa zinthu za dziko lino. Zokonda zanga ziri kumwamba. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti inunso muli chimodzimodzi, ngati inu muli pachiyanjano ndi Mulungu. Izo nzoona, kuti inu muli. Ife, mwa chikhulupiriro, talandila. Ife, mwa chikhulupiriro, tikukhulupirira Mulungu.

112 Mose, iye ankayenera kupanga chisankho. Ndiyeno iye ankayenera kutero, atatha kupanga chisankho, iye anamenyera chikhulupiriro, ndiye, pakuti iye sankawopa mkwiyo wa mfumu. Tsopano, mwaumunthu, iye anali nawo ufulu woti aziwopa mkwiyo. Iye anali nawo ufulu woti aziwopa mkwiyo wa mfumu, koma iye sanatero. Iye sanachite zimenezo, chifukwa iye anali nayo ntchito yoti ayichite, ndipo iye anali mu mzere wa ntchito. Ndipo iye sanasamale zomwe mfumu ankanena za izo. Iye anatenga njira Yake chimodzimodzi basi.

113 Tsopano, Farao, zoono, pamene iye anawona kuti wagonjetsedwa, ankafuna kuti amupatse Mose ndi ana... Iye anati, “Chabwino, ine ndikuwuzwa iwe chimene ine nditi ndichite. Inu nonse mungokhala mu dzikoli ndipo mupite uko muzikapereka nsembe kwa Mulungu wanu.”

114 Umo ndi mmene mdierekezi amagwirira ntchito. “O, iwe ukhoza kukhala wachipembedzo. Bwanji osapita ndi kukajowina mpingo wina? Iwe sukusowa kumachita zinthu zonse izi.” Mwamuna kunena kwa mkazi wake. . .

115 Mkazi nkuti, “Amunanga, ine ndapululumutsidwa. Ndasiya zozipentapenta zija, kapena zopaka mmilomo ndi zinthu. Ndasiya izi. Ndasiya zamaphwando. Ndasiya zinthu za mmagulugulu izi. Ine ndachokamo mu zimenezo! Ine ndiyika nthawi yanga mu kuwerenga Mawu, kusamalira pakhomo.”

116 “Tsopano, tawona, wokondedwa. Iwe, iwe ukhoza kukhala wachipembedzo, chabwino. Tsopano, tawona, i—iwe upite *uku*. Wapeza mpingo wolakwika.”

117 Ayi, iwe sunatero. Iwe uli mwa wolondolawo. Ngati iwe uli ndi mlaliki amene angalalikire izo kwa iwe, iwe uyenera kukhala nazo izo. Mufufuze kudutsa Malemba ndipo mukafufuze ngati izo ziri zolondola.

118 “O,” akuti, “upite *uku*. Iwo sama—iwo samachita zimenezo kuno. Mukuona? Iwo samachita izi kuno.” Njira yake ndi

imeneyo, “iwe ungopita mpaka apa,” koma iye sakufuna kuti iwe uchoke mu dzikolo. Umo ndi mmene mdierekezi amachitira. Iye samafuna kuti iwe uchoke mu zinthu za mdziko; amangolibweretsa dzikolo mu tchalitchi.

¹¹⁹ Tsiku lina, ndikubwera mu msewu, ine ndinayatsa walesi yanga. Ndipo apo panali—nyimbo, ndipo ine ndinakhala ndikuimvetserabe, ndipo ine ndinachita kutenga, pafupifupi, nyimbo yonseyo, ine ndisanathe kudziwa kuti inali mwamtheradi nyimbo yauzimu, kapena mdierekezi akuyesera kuti atsitsire pansi zinthu za Mulungu kuzifikitsa pa muyezo wa dziko. Inu simungathe kuchita zimenezo! Mulungu atichitire chifundo!

¹²⁰ Ine sindikusamala kuti ndi nyimbo zingati zimene Elvis Presley walembe, za nyimbo zonse zabwino zachipembedzo. Iye akadali wodzazidwabe ndi mdierekezi. Iye anatomiza ana ambiri ku gehena, ndi makanema onse amene ine ndikuwadziwa, mu dziko lonse mu tsiku lino. Pat Boone ndi ena onse a iwo, iye anali wa mpingo wa Khristu; ndipo Elvis Presley, wa Chipentekoste; iwowo ndi Yudasi Iskarioti, mmawonekedwe a amuna amenewo. Mdierekezi akuyesera kuti abweretse zinthu zapamwamba za Mulungu, kuti iwo akathe kuzisakaniza izo pansi *apa*. Anthuwo samayang’ana Mmwamba, *Ichi*. Iwo amangoyang’ana *apa*, ndikuti, “Chabwino, zonsezo ndi zofanana.” Izo si zofanana. Tulukani mu dzikolo.

¹²¹ Anati, “Inu mukhoza kungopita masiku pang’ono. Ndipo inu mupite, mukakhale mu dzikolo.” Ndithudi, iye ankadziwa kuti iwo abwereranso. Kenako iye anadzapeza kuti izo sizikanagwira ntchito, kotero iye anaganizira chinachake chosiyana. Iye anati, “Ine ndikuwuzani inu chimene muti mukachite. Inu mupite uko kulikonse kumene inu mukufuna kupita, koma inu muwasiye azikazi anu onse, ana anu onse, ndi ziweto zanu zonse, muzisiye *kuno*. Inu muzisiye izo kuno, ndipo mupite kunja uko.” Chifukwa, iye ankadziwa kuti iwo anali ndi chuma kumeneko, chimene chikanawakopa kuti azibwerera mmbuyo.

¹²² Ndipo ndi zimene mdierekezi amanena kwa inu. Basi bola ngati inu mwasiya zinthu zina za m’dziko zikulendewera pa inu, inu mumafunabe kuti muzisuta, inu mumafuna kuti muzimwa, inu mumafuna kuti muzivala ngati dziko. Zimenezo ndi zabwino basi mmene mdierekezi amafunira.

¹²³ Ine ndimamva zambiri za kubwerera mmbuyo. Ine sindikukhulupirira kuti kulipo kubwerera mmbuyo kochuluka monga mmene anthu amaganizira kuti kulipo. Iwo angosiya chuma chochuluka mu Igupto kuti chiziwakopera iwo mmbuyo, ndi zokhazo. Kubwerera mmbuyo si zomwe iwo amanena kuti ziri. Inu mwasiya zochuluka kwambiri m’dziko kumbuyo uko, zimene zikukukopani inu.

¹²⁴ M'bale, ine ndikukuuzani inu, pamene Israeli anakonzeka, pakati pa usiku, iwo anali nazo zonse zimene iwo anali nazo mu dziko lino, atazilongeza ndipo atakonzekera kuti azipita.

¹²⁵ Mulungu titumizireni ife chitsitsimutso chonga chimenecho. Ife talongeza chirichonse, ndipo takonzekera kuti tizipita. Kulira kwa pakati pa usiku kukubwera, "Tulukani inu panja mukakomane naye Iye." Zikanakhala bwino mukanalongedzeratu chirichonse. Inu kuli bwino musakhale ndi chirichonse, mdziko lino, choti chizikukoperani inu mmbuyo, zingwe zirizonse zoti zizikumangirirani inu pansi. Longedzani. Tiyeni tikonzekere. Ife tikupita.

¹²⁶ Ndipo inu mukudziwa chiyani? Ine ndikukuuzani inu, iwo anali owona kwambiri kwa Mulungu, mpaka Farao anatengeka kwambiri pakati pa usiku, iye anati, "Kazipitani! Kazipitani, ndipo muzipita. Mutenge chirichonse chimene inu muli nacho, ndipo muzipita!"

¹²⁷ Ndine wokondwa kwambiri kuti munthu akhoza kukhala moyo wa pafupi kwambiri ndi Mulungu, mpakana mdierekezi osadziwa kuti achite chiyani ndi iyeyo. Izo ndi zoon. Tulukani! Kazipitani! Zimumverani Mulungu!

¹²⁸ Mwa chikhulupiro, iye anawona lonjezo. Oponda matope, kapena osaponda matope, iye anatenga njira yake ndi onyozeka apang'ono a Ambuye. Farao anati, "mutenge zonse zomwe inu muli nazo ndipo muchokeke kuno! Ine sindikudziwa kuti ndichite nanu chiani inu." Iye anali woona kwambiri kwa Mulungu, mwa chikhulupiro.

¹²⁹ Chikhulupiro chimachita zozizwitsa, ngati inu mungakhale owona kwa Mulungu. Mwa chikhulupiro, ife tikumuwona Iye.

Nthawi yathu yatha; tadutsitsa nthawi.

¹³⁰ Koma, mwa chikhulupiro, mmawa uno, mukwezere mmwamba maso anu. Musawone zimene zakuzungulirani inu, dziko lamakono lino, koma muyang'ane ndi kumuwona Iye Amene anapereka lonjezo. Baibulo linati, "Ife sitikuziwona zinthu zonse mwangwiro tsopano, koma ife tikumuwona Yesu." Inu muziyang'ana pa Iye, mmawa uno, ndipo njira zanu zidzasinthidwa.

¹³¹ Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, mphindi chabe, kwa liwu la pemphero. Ambuye awonjezere madalitso Ake ku Uthengawu.

¹³² Muganizire mu mtima mwanu tsopano. Kodi inu mwakhala mukuyang'ana pa zinthu za mdziko? Mwa chikhulupiro, kodi inu mukumuwona Yesu? Kodi inu mukuyang'ana pa kutchuka kwanu, mpingo wanu? Chimene maimidwe anu ali ndi dziko? Kapena, kodi inu mukuwona Yesu Amene, mu chisoni, anadziika Yekha pa dzanja lamanja la Chifumu Mmwamba,

Amene anazunzika ngati wofera, wolungama chifukwa cha osalungama? Kodi inu simungakweze maso anu mmwamba ndi kuwuwona Mtengo uja wa Moyo kutsidyako? Mukatero, muusiye mtengo uwu wa sayansi ndi chidziwitso, ndipo mukamutumikire Iye?

¹³³ Kodi inu mungafune kuti mukumbukiridwe mu pemphero ine ndisanapemphere? Mukweze dzanja lanu, pa chosowa chirichonse chimene inu mungachisowe. Mulungu akudalitseni inu. Iye akuwona dzanja lanu lonse.

¹³⁴ Ngati ndinu wochimwa, mukweze maso anu mmwamba ndipo muyang'ane tsopano. Ngati inu mwakhala wosayanjanitsika, ngati inu mumakhala ndi makangano pang'ono ndi zinthu pang'ono, kodi zimenezo zikupanga kusiyana kotani? Inu mudzafa limodzi la masiku amenewa. Tsiku lake liti? Mwinamwake lero! Inu simukudziwa. Ora kuchokera pano, inu mukhoza kukakhala muli ku gehena, kapena inu mukhoza kukakhala Kumwamba. Koma inu muyenera kuti musankhe tsopano. Ngati chiripo chirichonse mmoyo mwanu chomwe sichiri cholondola, inu musankhe tsopano, mwa chikhulupiro.

¹³⁵ Inu mukuti, “Chabwino, ngati ine nditangom'bwezera iye! Ngati ine nditangom'bwezera iye!” Ziribe kanthu kuti iwo anachita chiyani, musankhe Moyo. Musankhe Moyo.

¹³⁶ Chifukwa, Yesu anati, “Ngati kuchokera mu mtima mwanu simungamukhululukire munthu aliyense mangawa ake, ngakhalenso Atate anu Akumwamba sadzakukhululukirani inu.” Koteru muzingoyandikana pafupi choncho. Ngati muli mangawa amodzi mu mtima mwanu motsutsana ndi munthu aliyense, wochimwa kapena woyera, inu muli pangozi ya moto wa ku gehena.

¹³⁷ Tsopano mukwezere diso lanu mmwamba. Kodi inu mukuwona chiyani, mdani wanu? Kapena, inu mukuwona Mpulumutsi wanu? Kodi inu mukuyang'ana chiyani mmawa uno?

¹³⁸ Ngati inu mukudwala, ndipo adokotala anu akunena kuti inu simungachire, mukwezere diso lanu mmwamba, pa mtanda, pamene Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa. Musayang'ane pa zimene adokotala akunena; iwo akugwira ntchito mwa sayansi. Chikhulupiro chimagwira ntchito mu gawo la Mzimu ndi Mulungu. Tiyeni ife tiganizire za zinthu izi tsopano pamene inu mwakweza dzanja lanu. Mulungu wawaona iwo.

Tiyeni tipemphere.

¹³⁹ O, Mulungu Wamuyaya, mu kachetechete wa kupembedza uku tsopano, Uthenga utatha kudutsa, musalore mbewu izo za Mawu Anu, Ambuye, zikagwere pa nthaka ya miyala. Musalole

Uthenga, Ambuye, ukagwere mu zisonga, minga, kuwopa kuti zosamalira za moyo uno (monga Loti) zingawutsamwitse iwo, pamapeto ake, nkukhala zokataidwa. Koma, O Mulungu wodala, mulole iyo ikagwere panthaka yabwino, pa nthaka yachonde, pa mitima yofunitsitsa. Ndiponso pa wanga, inenso, Ambuye, kuti tonsefe tikathe kuyang'ana kudutsa pa kalilole wa Mulungu, ndipo tikawuwone Mpingo wokanidwa wa Ambuye Yesu, anthu okanidwa, njira yokanidwa, ndipo mukalole kuti ife tikayende mu njira ya ulemerero iyi.

¹⁴⁰ Monga Mose, iye sankadziwa kumene iye anali kupita. Anthuwo sankadziwa komwe iwo anali kupita. Iwo sankadziwa kuti azilowera kuti. Iwo anangowuyambapo.

¹⁴¹ Ndipo O Ambuye Mulungu, pamene nyimbo yokongola iyi ikuseweredwa, mwa chikhulupiroro ife tikutha kuliwona Dzikolo kutali uko. Mulole kuti zikhale pomwe pano, kuti amuna ndi akazi ali muno asaganizire za zomwe dziko liti lizikanena, kapena momwe iwo akuyendera. Mulole iwo akangodzuka mu mzimu wawo, ndi kumapita.

¹⁴² Mose ankatsatira Kuwala, ndipo Iko kunamutsogolera iye mpaka ku dziko la lonjezo. Osadziwa komwe iye anali kupita, koma iye ankagoyenda mu Kuwala, akupita ku dziko ilo lomwe linali labwino kuposa masana.

¹⁴³ Perekani, Ambuye, lero, kuti ambiri pano akayende mu Kuwala kwa Lemba ndi mu chiyanjano cha Mzimu Woyera, ndi Mpingo; Mpingo, Oyamba-kubadwa, ana obadwa kumene amene amulandira Khristu, ndipo adzazidwa ndi Mzimu Woyera, akutsogozedwa ndi Mzimu. Mulole ife tizikayenda mu chiyanjano ichi, limodzi, pozungulira zinthu za Mulungu; tikumutumikira Iye mu ubatizo, momvera ku imfa Yake, kuyikidwa mmanda, ndi chiukitsiro. Mulole ife tikamutumikire Iye mu kulamulira Kwake, "Mukadikirire inu ku Yerusalemu kufikira inu mutadzazidwa ndi Mphamvu yochokera Mmwamba." Mulole ife tikamutumikire Iye mu machiritso Auzimu, kupempherera odwala. Mulole ife tikamutumikire Iye mu mgonero, kunyema kwa mkate, ndi mtima umodzi, tikuchita chiyanjano pozungulira Mawu a Mulungu. Mulole ife tikamutumikire Iye mu zinthu Zake zonse Zauzimu, mpakana Dzikolo likayambe kumawonekera. Perekani izi, Ambuye. Mumve pemphero lathu, pamene ife tikuzipereka zonse izi kwa Inu tsopano, mu Dzina la Ambuye Yesu.

¹⁴⁴ Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, mwakachetechete, pang'onopang'ono, tiyeni tingoimba nyimbo iyi. Tsopano uku ndi kupembedza. Uthenga watha. Aliyense asachokepo. Mungokhala chete. Tiyeni tipembedze.

¹⁴⁵ Uthenga ndi wokonza. Muganizire tsopano zomwe inu mwazichita, zimene inu mukanayenera kuti muchite, chimene chakupangani kuti inu mukhale chimene inu muli lero. Chimene

chimakupangani inu kutsutsika, lero, ndi chifukwa chakuti inu munachita chinachake dzulo. Kodi mawa chidzakhala chiyani? Chikonzeni icho lero, ndipo mudzakhala mfulu mawa. Mwawona? Inu muyenera kupanga chisankho. Kodi inu mungachite bwanji izo? “Mwa chikhulupiriro, ine tsopano ndikumacula chirichonse. Ine tsopano ndikumacula, ndipo tsiku lina ine ndidzapita Kumeneko.”

Mokoma pang’ono ndi pang’ono
Ife tidzakakomana pa- . . .

Muzingomupembedza Ambuye mu mzimu wanu tsopano.

Mokoma pang’ono ndi pang’ono,
Ife tidzakakomana nawo Mpingo wonyozedwa
uja. (Kudutsa movutikira, koma ife
tidzakakomana tsiku lina.)

Kwa Atate athu achifundo Mmwamba,
Ife tidzakupereka mtulo wathu wa
kupembedza,
Kwa mphatso ya ulemerero ya chikondi Chake,
Ndi madalitso omwe amakweza athu . . .

Ndi onyozedwa apang’ono a Ambuye, mwa chikhulupiriro, ine ndikusankha.

Mokoma, (mokoma) pang’ono . . . (pang’ono ndi
pang’ono)
Tidzakakomana pa gombe lokongolalo;
(pang’ono ndi pang’ono)
Mokoma (mokoma) pang’ono ndi pang’ono,
Tidzakakomana pa gombe lokongola lija.

Kuli Dziko lomwe liri . . .

Muzingomupembedza Iye. Uku ndi kupembedza.

. . . chikhulupiriro ndikukhoza kuwona,

Mwa chikhulupiriro ine ndikupanga kusankha kwanga.

O, Atate akudikirira . . .

¹⁴⁶ Ine ndikuwawona onse a Ambuye cha Kumeneko; M’bale George, M’bale Seward, oyera onse.

. . . malo okhalako Kumeneko. (Inde, Ambuye!)
Mokoma . . .

¹⁴⁷ Bambo ake, Howard, Edward, abwenzi onse oyera amene anatenga Njira, mmbuyo uko, kale kale.

Mokoma (Inde, Ambuye!) pang’ono ndi
pang’ono (pang’ono ndi pang’ono),
Tidzakakomana pa gombe lokongola ilo.

Tidzakaimba pa loko-... (O Mulungu!)
Nyimbo zanthetemya za odalitsidwa,
(Ulemerero kwa Mulungu!)
... sitidzamvanso chisoni,
Opanda nkhawa kwa madalitso a Malo a
mpumulowo.
Mokoma, mokoma pang'ono ndi... (pang'ono
ndi pang'ono)
Tidzakakomana pa loko-...



MWA CHIKHULUPIIRO, MOSE CHA58-0720M
(By Faith, Moses)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Julaye 20, 1958, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2015 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org